Kuganizira za Malamulo

Gwiritsani ntchito tsambali kuti muganizire lamulo lomwe mumaona kuti ndi lovuta. Mungagwiritsenso ntchito tsambali pokambirana ndi makolo anu.

N'chifukwa chiyani mumaona kuti lamulolo ndi lovuta?

Kodi pali zinazake zomwe mukuona kuti **mukhoza** kugwirizana nazo m'lamuloli?

Kodi mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani makolo anu anakhazikitsa lamuloli?

Kodi pali zinazake zomwe mukuona kuti makolo anu sanaziganizire pokhazikitsa lamuloli? Ngati zili choncho, kodi zinthu zake ndi ziti?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kodi mungakonde kuti alisinthe pati lamuloli?

Ngati mutapempha makolo anu kuti asinthe lamulolo, kodi mukuona kuti angayankhe bwanji?

☐ “Ayi, sitingasinthe.”

☐ “Mwina, tingasinthe.”

☐ “Palibe vuto.”

Kodi mukuganiza kuti n’chifukwa chiyani angayankhe choncho?

Kodi mungatani kuti makolowo asiye kudera nkhawa zimenezo, ngakhale kuti sangasiye kamodzin’kamodzi? (Zokuthandizani: Zimene mungachite zingathandize kwambiri kuposa zimene munganene.)

Kodi mukuganiza kuti makolo anu akudera nkhawa za chiyani?

Tayerekezerani kuti inuyo muli ndi mwana wachinyamata. Kodi inuyo mukanakhazikitsa lamulo lokhala ngati limenelo? Ngati ndi choncho, kodi mungakhazikitse lamulo liti ndipo n’chifukwa chiyani mungachite zimenezi?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

KODI MWACHITA ZINTHU ZINAZAKE ZOMWE ZINGATHANDIZE KUTI MAKOLO ANU AZIKUKHULUPIRIRANI?

Tchulani zinthu zina zomwe munachita zimene zinachititsa kuti makolo anu **asiye** kukukhulupirirani.

_____

_____

_____

_____

_____

Tchulani zinthu zinazake zimene munachita zomwe **zinathandiza** kuti makolo anu azikukhulupirirani.

_____

_____

_____

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Kodi mukuona kuti mwachita zinthu zokwanira moti panopa mutha kukambirana ndi makolo anu za lamulo limene mumaliona kuti ndi lovuta?

Ngati mukuona kuti mukufunika kudikira kaye, kodi ndi zinthu ziti zimene mukuona kuti mukuyenera kuchita kuti makolo anu azikukhulupirirani kwambiri?

ZIMENE ZINGAKUTHANDIZENI: Aonetseni makolo anu zimene mwalemba patsambali ndipo ligwiritseni ntchito pokambirana nawo.

Mukamakambirana ndi makolo anu, kumbukirani mawu a m'Baibulo akuti: "Kuyankha modekha kumabweza mkwiyo, koma mawu opweteka amayambitsa mkwiyo."—Miyambo 15:1.

KODI MUKUDZIWA? Mfundo zapatsambali zingakuthandizeninso mukadzafuna kukambirana ndi abwana anu za malamulo enaake akuntchitoko.

"Kumvera malamulo a makolo anu kuli ngati kubweza ngongole kubanki. Mukamatsatira malamulo awo mokhulupirika, iwo angayambe kukukhulupirirani kwambiri."—Mawuwa ndi ochokera m'buku lakuti *Mayankho a Zimene Achinyamata Amafunsa,* Buku Lachiwiri.

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania